PHUNZIRO LA 46

1. Kodi Yesu anachokera ku mtundu uti?
-Yesu anachokera ku mtundu wa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

2. Kodi Yesu anachokera ku mtundu wanji ndipo mfumu yanji yayikuru ya ku Yuda?
-Anachokera ku mtundu wa mfumu Davide.

3. Kodi dzina lakuti Kilisito likumasulira chiyani?
-Dzina lakuti Kilisito likutanthawuza kuti Iye anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Mneneri Wamkulu kwambiri.
-Dzina lakuti Kilisito likutanthawuzanso kuti Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Wamsembe wamkulu kwambiri.
-Dzina lakuti Kilisito likutanthawuzanso kuti Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Mfumu wamkulu kwambiri.

4. Kodi Yosefe ankaganiza chiyani chifukwa chakuti Mariya anali ndi khanda?
-Yosefe ankaganiza kuti Mariya anakhala pa malo amodzi ndi mamuna wina.

5. Kodi Mariya anakhala pa malo amodzi ndi mamuna aliyense?
-Iyayi.

6. Kodi Mariya anabereka bwanji mwana?
-Mulungu Mzimu Woyera anapanga zodabwitsa, ndipo Mariya anabereka mwana.

7. Kodi Yosefe anamutengera ku nyumba kwache Mari-

ya ngati mkazi wache?
-Inde.

8. Kodi chifukwa chiyani Yesu ankatchedwa kuti Emanu-welo?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi ame-ne ankabwera kudzakhala ndi anthu.

-Nthaŵi yakuti Mariya abereke mwana itakwana, ana-bereka mwana wamamuna.
-Mariya anabereka mwana wamamuna ndikumukutira mu nsaru, ndipo anamuyika mu chodyera ng'ombe, chifukwa chakuti kunalibe chipinda china chilichonse.

-Mariya ndi Yosefe anamutcha mwanayo dzina lakuti Yesu.

-Ngakhale kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi, Iye anayikidwa mu chodyera ng'ombe atabadwa.

-Kodi Yesu anabadwira mdziko lanji?
-Isirayeli.

-Kodi nanga Yesu anabadwira mu mzinda wanji?
-Betelehemu.

-Yesu anabadwa kuti atipulumutse ife ku mphamvu ya tchimo.

- Yesu anabadwa kuti atipulumutse ife ku mphamvu ya imfa.

- Yesu anabadwa kuti atipulumutse ife ku mphamvu ya Satana.



Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:21-23

21-Chomcho anadzuka, ndikumutenga mwanayo pamodzi ndi mayi ache, ndikupita naye mu dziko la Isirayeli.
22-Koma Yosefe atamva kuti Alikaleyasi ndi ame-ne anali mfumu ku Yuda m'malo mwa bambo ache, Herodi, iye anawopa kupita kumeneko. Chifukwa chakuti iye anachenjezedwa m'maloto, iye anapita ku Galileya,
23-kumeneko anapita kukakhala mu mzinda wina wotchedwa kuti Nazareti. Chomcho anakwanilitsa zimene zinalankhulidwa kudzera mwa mneneri kuti: "Adzatchedwa Mnazareni."

-Yosefe, Mariya, ndi Yesu anabwelera ku dziko la Isirayeli.

-Kodi Yosefe anamutengera mu mzinda wanji Mariya ndi Yosefe?
-M'dziko la Isirayeli mu mzinda wa Nazareti.

-Yesu, Mpulumutsi ankakhala mu mzinda wa Nazaleti ngati m'mene analonjezera Mulungu kudzera mwa ane-neri kalekale.

-Mulungu amasunga malonjezo ache.

-Mulungu saphwanya malonjezo ache.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu Atate anamupulumutsa Yesu?
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate anamutumiza Yesu kuti aŵapulumutse anthu ku mphamvu ya tchimo.
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate anamutumiza Yesu kuti aŵapulumutse anthu ku mphamvu ya imfa.
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate anamutumiza Yesu kuti aŵapulumutse anthu ku mpnhamvu ya Satana.

-Kodi Mulungu anatha kumupulumutsa Yesu?
-Inde.

-Kodi Herodi anatha kumupha Yesu?
-Iyayi.

-Mfumu Herodi atamwalira, Mulungu anatumizanso mngero kukalankhula kwa Yosefe.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:19-20

19-Herodi atamwalira, mngero wa Ambuye ana-wonekera kwa Yosefe m'maloto ku Iguputo
20-ndipo anati, "Dzuka, tenga mwanayo pamodzi ndi mayi ache ndipo upite mu mzinda wa Isirayeli, pakuti iwo amene amafuna kutenga moyo wa mwanayu, amwalira."

-Kodi mngero anamuwuza chiyani Yosefe?

-Mngero anamuwuza Yosefe kuti mfumu Herodi anamwalira.

-Mngero anamuwuzanso Yosefe kuti amutenge Mariya ndi Yosefe ndikubwelera naye ku Isirayeli.



-Mulungu anatumiza Mpulumutsi kuti adzatipulumutse ife ngati mmene anatilonjezera.

-Yesu Mpulumutsi anabadwa pa dziko la pansi ngati mmene Mulungu analonjezera.

-Yesu anabadwira mu mzinda wa Betelehemu ngati mmene Mulungu analonjezera kudzera mwa Aneneri kalekalelo.

-Yesu atabadwa mu mzinda wa Betelehemu, anthu an-zeru anabwera mu mzinda wa Yelusalemu.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:1-2

1-Yesu anabadwira m'mudzi wa Betelehemu, m'dziko la Yudeya, pa nthaŵi imene Herodi anali mfumu wa dzikolo. Pa nthaŵi imeneyo, anthu ena anzeru a ku m'maŵa anabwera mu mzinda wa Yelusalemu
2-ndipo anafunsa, "kodi mwana amene wabadwa kuti akhale Mfumu ya Ayuda ali kuti? Tinayiwona nyenyezi yikuturuka ku m'maŵa ndipo tabwera kuti ti-dzamupembedze Iye."

-Kodi amuna anzeruŵa ankamufunafuna ndani?
-Yesu amene anamutcha kuti mfumu ya Ayuda.

-Mfumu Herodi atadziŵa kuti amuna a nzeru ankamu-funafuna Yesu, iye anavutika kwambiri mu mtima mwache.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:3

3-Mfumu Herodi atamva zimenezi, zinamupwete-ka kwambiri mu mtima mwache, nawonso anthu ku Yelusalemu zinaŵapweteka m'mitima mwawo.

-Kodi chifukwa chiyani mfumu Herodi anavutika kwambiri mu mtimwa mwache?
-Chifukwa chakuti mfumu Herodi ankawopa kuti mwina mwache mfumu imene ankayifufuza anthu a nzeru aja idzamulanda iye ufumu wache.

-Chifukwa chakuti mfumu Herodi anavutika kwambiri mu mtima mwache, iye anaŵayitanitsa pamodzi akuluakulu amsembe ndi aphunzitsi a malamulo.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:4-6

4-Mfumu Herodi anaŵayitanitsa akuluakulu onse a msembe ndi aphunzitsi a malamulo a Mose ndipo anaŵafunsa kuti, “Kodi paja amati kuti Mpulumutsi adzabadwira kuti?”
5-Iwo anayankha kuti, “mu mzinda wa Betelehemu m’dziko la Yudeya, pakuti izi ndi zimene analemba Mneneri:
6-“Ndipo iwe, Betelehemu wa m’dziko la Yudeya siwulinso wamng’ono konse pakati pa akuluakulu olamulila dziko la Yudeya. Pakuti kwa iwe kudzachokera Olamulira amene adzawete anthu anga a Isirayeli.

-Kodi mfumu Helodi anaŵafunsa chiyani akuluakulu amsembe ndi aphunzitsi a malamulo aja?
-Anaŵafunsa za kumene kunali Kilisitu, mfumu ya Ayuda imene inabadwayo.

-Kodi akuluakulu amsembe ndi aphunzitsi a malamulo aja anayankha chiyani?
-Iwo anamuwuza iye kuti Kilisitu anabadwira ku Betelehemu.



-Kodi Herodi anachita chiyani pamene amuna anzeru aja anaganiza zosabwelera kwa iye?

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:16-18

16-Mfumu Herodi atazindikira kuti wapusitsidwa ndi amuna anzeru aja, anakwiya kwambiri, chomcho anaŵatumiza anthu ku Betelehemu ndi ku midzi yonse yozungulira, kuti akaphe ana onse amuna a zaka ziŵiri ndi ochepera ake. Zaka zimenezi anaziŵerengera potsata nthaŵi imene amuna anzeru aja anayiwonera nyenyezi ija.
17-Pamenepo zinachitika zimene analankhula mneneri Yeremiya kuti:
18”Mawu akumveka ku Lama, kulira ndi kukuwa kwakukuru. Lakelo akulilira ana ache. Akukana kuti apembedzedwe. Pakuti ana ache onse amwalira.”

-Mfumu Herodi analamula kuti ana onse amuna a zaka ziŵiri ndikuchepera apo amene akukhala ku Betelehemu ndi ku midzi yonse yozungulira mzindawo, aphedwe.

-Satana ankadziŵa kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi pa dziko la pansi.

-Satana ankadziŵa kuti Mpulumutsi adzabwera kudzamugonjetsa iye.

-Chomcho satana anayesa kuti amuphe Yesu.

-Satana anamuwuza mfumu Herodi kuti amuphe Yesu.

-Kodi Mulungu Atate anamupulumutsa Yesu?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani mfumu Herodi ankafuna kumupha Yesu?
-Chifukwa chakuti mfumu Herodi sankafuna kuti papezeke mfumu wina wotenga udindo wache.

-Kodi ndani amene anapereka maganizo kwa Herodi ofuna kumupha Yesu .
-Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Satana ankafuna kumupha Yesu?
-Chifukwa chakuti Satana sankafuna kuti Yesu aŵapulumutse anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satanayo.

Apa pali fanizo:

-Kodi munthu akakhala ndi akapolo ambiri, amafuna kuti munthu wina abwere kudzaŵatenga akapolo achewo?
-Iyayi, samafuna kuti munthu wina abwere kudzaŵatenga akapolo achewo.

-Kodi mfiti ikakhala ndi akapolo ambiri, imafuna kuti munthu wina abwere kudzaŵatenga akapolo achewo?
-Iyayi.

-Satana amafuna kuti adziŵasunga anthu ache onse ngati akapolo ngati m'menenso imafunira mfiti kuti idzisunga akapolo ache.

-Ichi ndi chifukwa chimene ankafunira Satana kuti amuphe Yesu.

-Satana sakufuna kuti aŵataye akapolo ache amene ali pasi pa ulamuliro wache.



-Kodi akuluakulu amsembe ndi aphunzitsi a malamulo aja anazidziŵa bwanji zimenezi?
Anazidziŵa chifukwa chakuti anaziŵerenga Bayibulo, mawu a Mulungu.

-Akuluakulu amsembe ndi aphunzitsi a malamulo aja anaŵerenga M'bayibulo kuti Mfumuyi idzabadwira ku Betelehemu ngati m'mene analonjezera Mulungu.

-Kenako mfumu Herodi anaŵatuma amuna anzeru aja kuti apite mu mzinda wa Betelehemu kuti akayifufuze mfumuyo.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:7-11

7-Kenako mfumu Herodi anaŵayitana anthu a nzeru aja mwa m'tseri naŵafunsisitsa iwo za nthaŵi yeniyeni imene nyenyezi inaŵawonekera.
8-Pambuyo pache anaŵatumiza ku Betelehemu ndipo anaŵawuza kuti, "Pitani ndipo mukafufuze bwino za mwanayo. Mukakamupeza, mudzandiwuze kuti nanenso ndidzapite kukamupembedza iye."
9-Anthu aja ataŵamva mawu a mfumu aja, ananyamuka; ndipo nyenyezi ija inaŵawonekeranso ku m'maŵa, inaŵatsogolera iwo, mpakana inayima pamwamba pamene panali mwanayo.
10-Ndipo iwo powona nyenyeziyo, anasangalala kwambiri.
11-Ndipo atafika ku khola la ng'ombeko, anawona mwanayo ali ndi Mariya, mayi ache, ndipo anagwada pansi nampembedza iye; namasula chuma chawo, namupatsa iye mitulo ya golide, ubani ndi mure.

-Kodi amuna anzeru aja anachita chiyani pamene iwo anamupeza Yesu amene ankamutcha kuti mfumu ya

Ayuda uja?
-Anamupembedza iye.
-Anamupatsanso mitulo.

-Kodi Mulungu anakwiya chifukwa chakuti anthu anzeru aja anamupembedza Yesu?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanakwiye anthu anzeru aja atamupembedza Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.

-Yesu ndi Mulungu komanso ndi munthu weniweni.

-Kodi anthu anzeru aja anabweleranso ku Yelusalemu kuti akalankhulanenso ndi mfumu Herodi?

Tiyeni tiŵerenge Mateyo 2:12

12-Ndipo Mulungu anaŵachenjeza iwo m'maloto kuti asadzelerenso kwa mfumu Herodi, chomcho anadzera ku njira ina pobwelera kwawo.

-Mulungu anaŵawuza amuna anzeru aja kudzera m'maloto kuti asabwelerenso ku Yelusalemu kuti akalankhulanenso ndi Herodi.

-Chomcho amuna anzeru aja anabwelera kwawo kupitira ku njira ina.

-Amuna anzeru aja atachoka, Mulungu anatumiza mngero kuti akalankhule kwa Yosefe.

Tiyeni tiŵerenge Mateyu 2:13-15



13-Amuna anzeru aja atachoka, mngero wa Mulungu anamuwonekera kwa Yosefe m'maloto ndipo anati, "Nyamuka ndipo umutenge mwanayu pamodzi ndi mayi ache, uthawile ku Iguputo. Ukakhale kumeneko mpaka pamene ndidzakuwuzire, pakuti Herodi adzakhala akumufunafuna mwanayu kuti amuphe."
14- Yosefe anadzuka, ndikutenga mwana ndi mayi ache ndipo ananyamuka usiku omwewo kupita ku Iguputo,
15-kumene anakakhala mpaka Herodi atamwalira. Chomcho anakwaniritsa zimene Ambuye analankhula kudzera mwa mneneri kuti:"Ndinamuyitana mwana wanga kuti atuluke mu Iguputo.'

-Kodi mngero anamuwuza chiyani Yosefe kudzera m'maloto?
-Amtenge Mariya ndi Yesu ndipo athawe.

-Kodi mngeroyo anamuwuza Yosefe kuti antenge Mariya ndi Yesu kuti apite ku dziko lanji kuti mfumu Herodi asamuphe mwanayo?
-Ku Iguputo.

-Yosefe atadzuka, anamutenga Mariya ndi Yesu kupita nawo ku dziko la Iguputo.

-Yesu anatengedwa kupita ku dziko la Iguputo ngati m'mene analonjezera Mulungu kalekale kudzera mwa aneneri.

-Kodi chifukwa chiyani Yosefe anamutenga Yesu ndikupita naye ku Iguputo?
-Chifukwa chakuti mfumu Herodi ankafuna kumupha Yesu.